

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

MALANGIZO NDI CHILIMBIKITSO KUCHOKERA M'BAIBULO
KUPITA KWA AMENE AKULALIKIRA UTHENGA WABWINO

KAKOBIRI KA MKAZI WAMASIYE

(Nkhani iyi ikulongosola zimene ananena Yesu pa Marko 12:41-44).

Yesu anayenda mu khonde la kachisi ndipo anakhala panso, akuyang'ana anthu. Zoonadi, panali anthu osiyanasiyana. Panali amuna kunja kwa kachisi amene amapanga bizinesi, kugula ndi kugulitsa, namawadyera masuku pamutu anthuwo amene amayenera kudzagula zifuyo. Ayuda ochokera kumadera akutali, amene anali otuwa ndiponso otopa chifukwa cha ulendo, amakonzekera kubweretsa nsembe zawo kwa ansembe. Afarisi amayendayenda monyada pakati pa chikhamu cha anthuwo, ndi kumapemphera ndi mau okweza, komanso kumayamikira za ntchito zao zabwino. Ena, amene amadziona kuti ndi osayenera kukhala m'nyumba ya Mulungu, amaona kuwala kwa kupembedza pamene amapereka zopempherera zao ndi nsembe zao kwa Yehova Mulungu.

Yesu anaona zochitikazo ndipo anakhudgidwa mumtima mwake popeza iye amaona kuseli kwa zochitikazo nazindikira zolingalira za mtima wa munthu wina aliyense. Iye amadziwa ndithu za mu mkati mwa mtima wa aliyense komanso cholinga chimene amachitira zinthu. Iye amaona kudzichepetsa mwa ena ndiponso

kudzikuza mwa ena. Iye amaona kudzilungamitsa ndi undekha mwa ena pamene amaonanso mtima wodzichepetsa, wolapa ndi wodzikana mwa enanso.



Lipenga linalira. Yesu ndi anthu ena ambiri anatembenuka kuti aone Mfarisi wina akuyika ndalama zochuluka mu malo operekera ndalama a mu kachisi. Kunja kwa kachisi, panali mbale zambiri zomwe cholinga chake chinali

kulandiriramo zopereka kuchokera kwa anthu. Yesu anayang'anitsitsa ndi chidwi pamene banja lina laling'ono linapereka ndalama zawo mwansanga ngati kuti akuchita manyazi ndi kuchepa kwa ndalamazo. Iye anaona kuti anthu ambiri amene anavala mwapamwamba omwe ankapereka ndalama zochuluka kwambiri.

Pamene Yesu amayang'ana, iye anaona mzimayi wina wamasiye komanso wosauka kwambiri akuponya tindalama tiwiri tokwanira kakobiri mu mbale ya chopereka. Kakobiri kanali kandalama kochepetsa kapena Ayuda amagwiritsa ntchito ndipo mtengo wake unali wochepa kwambiri. Iye anamuyang'ana maiyu mwachikondi komanso mwachifundo. Maiyu anapereka kwa Mulungu Atate wake ndalama yomalizira yeniyeni imene anali nayo. Analibenso ndalama ina yakuti akanagulira chakudya cha tsiku limenelo, komabe anapereka china chilichonse ndi mtima wopembedza komanso wodzikhuthula.

Yesu anayimirira nayitana ophunzira ake kuti abwere. Pamene ophunzirawo anasonkhana pamodzi, Yesu anayamba kulankhula. Gulu la anthu limene linali pafupi ndi Yesu linayamba kuchuluka koma

(Yapitirira pa tsamba 2)

Mawu a Mkonzi

3

Kusanthula Mau a
Mulungu:
Chakhumi mu Baibulo
ndi Kupereka

4

Nkhani Yotsagana Nayo:
Chakhumi mu Baibulo
ndiponso Chopereka

5

Mafunso ndi Mayankho

7

Kodi Mukudziwa?

Mau a pa Nyengo yake

8

ZIMENE BAIBULO

Limaphunzitsa za...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;

Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chiyero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;

Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;

Akol. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;

1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chiyero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;

1 Akor. 7:10-11

Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;

Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba 1)

chidwi chawo chinayamba kuchoka chifukwa cha zinthu zosayembekezera zimene amamvazo. “Mkazi wamasiye amene waumphawi anaponya zambiri koposa onse akuponya mosungiramo.” Pamene anthuwo amayang’ana pa Yesu modabwa, Iye analongosola nati: “Pakuti anaponyamo onse mwa zochuluka zao; koma iye anaponya mwa kusowa kwake zonse anali nazo, inde moyo wake wonse.”

Nkhani ya Yesu ndi kakobiri ka mayi wamasiye iwoneka yochepa komabe ili ndi phunziro lamphamvu limene likutionetsa mmene Mulungu amaonera zopereka ngakhale lero. Mulungu amayang’anabe ndipo akuonabe chuma chochuluka cha olemera komanso kusowa kwa osauka. Iye amaona zimene zimachitika pagulu ngakhale kuseli. Iye amadziwa mtima umene umakhala kuseli kwa choperekacho, ngati akupereka kuti awonedwe ndi anthu kuti ayamikiridwe kapena kupereka mwachikondi ndi kudzipereka kwa Mulungu.

Mulungu amalemekeza mtima woperekerawo kwambiri kusiyana ndi choperekacho. Iye amakhudzidwa ndi mtima wopereka modzikhuthula kwa Mulungu ngakhale munthuyo ali osauka. Ngakhale zopereka zazikuluzikulu zimathandizira kwambiri ntchito ya Mulungu, chuma sichiyikidwa kumwamba malingana ndi kuchuluka kwake kapena kuti zaperekedwa mulingo wotani koma chifukwa cha mulingo wa kudzikhuthula kwa woperekayo. Anthu olemera ambiri akupitirirabe kupereka monga mwa kuchuluka kwa chuma chawo ndipo osauka ambiri sapereka nkomwe chifukwa cha kusauka kwawo. Yesu akuyitana onse kuti akhale nawo mtima ndi moyo wopereka ngati wa mayi wamasiye wosauka uja. Perekani modzikhuthula kaya ndinu olemera kapena osauka. Perekani zopereka zanu osati chifukwa cha kuchuluka koma chifukwa cha kudzikhuthula kwanu.

—mws

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Uthenga Wabwino wa Choonadi ndi uthenga wa mkalata umene umasindikizidwa m’dzina la Ambuye kwa anthu onse ku maiko onse ndi cholinga chofuna kuwakhazikitsa ndi kuwalimbikitsa mu choonadi cha Mau a Mulungu. Kalata uyu akuphunzitsa ndi kulimbikitsa zoono za Baibulo zimene zakhazikitsidwa kuyambira pa nthawi ya Khristu ndi ya atumwi.

Mau a Mulungu ndi okhawo amene ali muyeso wovomerezeka wa chikhulupiriro. Amaphunzitsa chipulumutso ndi mamasulidwe kuchokera ku uchimo kudzera mu ntchito ya maombedwe ya mwa Yesu Khristu; komanso kudzazidwa ndi Mzimu Woyera kumene kumatsatirapo. Ndipo kumatithandiza kuti titsogolere, tiwongolere ndi kuwapatsa ena mphamvu; komanso tikhale ndi chiyero choonekera pa gawo lililonse la moyo wa munthu kuphatikizapo mgwirizano ndi umodzi wa anthu a Mulungu. Utumiki wovomerezeka wa kwa Mulungu uli mu mwa anthu amene ubale wao wachikondi wazikika pa choonadi.

Akonzi: Michael & René Smith

KUTI MULANDIRE NAWO KALATAYI

Uthenga Wabwino wa Choonadi ndi uthenga wa kalata umene timasindikiza miyezi itatu iliyonse molingana ndi chitsogozo cha Ambuye. Kuti mulandire nawo kalatayi mwaulere pa email, pitani pa intaneti ndipo mutipeza pa www.thegospeltruth.us. Muli omasuka kutitumizira maina ndi ma email a anthu amene akufuna kulandira nawo kalatayi. Mainawa muwatumize kwa mkonzi.

KUTI MUTIPEZE

Uthenga Wabwino wa Choonadi imasindikizidwa mu maiko osiyanasiyana kuti igawidwe m’maikowo.

Ntchito yosindikiza kalatayi komanso mautumiki ena ochitika ndi ofesi yathu pothandiza kufalitsa uthenga wabwino amathandizidwa ndi zopereka zaufulu zoperekedwa mdzina la mpingo wa Mulungu.

The Gospel Truth, P.O. Box 2042, Nixa, MO 65714 USA
editor@thegospeltruth.org

Mau a Mkonzi



Kodi munthu adzalanda za Mulungu? Ndipo inu mundilanda Ine. — Malaki 3:8

Malaki mneneriyo anafunsa anthu ngati amalanda za Mulungu ndipo ndipo kenaka anawauza kuti zoonadi iwo amalanda za Mulungu mwa chakhumi ndi zopereka. Alaliki ambiri amene amafuna kuwadyera anthu ndalama amayisokoneza ndi kuyipotoza ndime imeneyi. M’maiko mwina mmene ndinayenda, ndime imeneyi ndiye tsinde la utumiki m’mpingo yambiri – perekani chakhumi, perekani chakhumi, perekani chakhumi.

Katundu amene ndili naye ulendo ndiye kumanga pa maziko a kalata ya ulendo wapita pamene timaphunzitsa za mapangano awiri. Chakhumi ndi chiphunzitsa cha ku Chipangano Chakale chimene chinathetsedwa ndipo mmalo mwake pali pangano loposa limene kupereka ndi kwaifulu ndiponso kuchokera mu mtima. Ndikadakonda kuti anthu awone ndi kuzindikira madalitso enieni ndiponso mphotho ya kutumikira mwaifulu komanso kupereka. Kupereka ukhoza kukhala mutu wovuta kuti munthu wa Mulungu aphunzitse. Poopa kuti mwina anthu adziganiza kuti angofuna kudzilemeretsa yekha. Mutuwu ndi wofunikira ndi woyenera pakati pa oyera mtima ngakhale lero.

Sitimangidwanso ku chakhumi koma udindo wathu wa kupereka ukhalapobe. Anthu ena amapereka pang’ono kapenanso osapereka nkomwe popeza sanamangidwe ku kupereka chakhumi, koma ngakhale zili choncho, tiyeni tikumbukire zimene Paulo anatilibikitsa nazo kuti: “Pakuti adakuitanani inu, abale, mukhale mfulu; chokhacho musachite nao ufulu wanu chothandizira thupi, komatu mwachikondi chitiranani ukapolo.” (Agalatiya 5:13).

Pali zofunikira zambiri mu ntchito ya Mulungu koma malo ndi ochepa kuti tizilembe zonsezo. Ndingokambapo mwachidule mfundo zina zokhudza kupereka ku utumiki. Udindo woyamba pa gawo la kupereka umayamba ndi uyo amene amatidyetsa chakudya chauzimu lamulungu lililonse – amene ali mbusa. Zimakhalapo nthawi pamene mbusa amakhala kuti anachokapo. Nkofunika kuti mpingo usayiwale udindo wake m’nthawi zimenezo.

Alaliki ndi ma mishonare alibe gulu la anthu limene limafuna kutenga udindo kuti lidziwandiza. Kumafunikira ndalama zambiri kupita kunja kukalalikira ndi kubweranso kumudzi, komanso iwo amayenera kuti alipire mabilu ngati magetsi, madzi monga mmene amachitira wina aliyense. Zopereka zongopereka kamodzi komabe nkumaperekabe pakapita nthawi ndi zothandiza kwambiri. Pamene mbusa alandira chopereka chochuluka dziwani kuti iye mwina wakhala akuvutika osalandira kanthu kapena kungolandira zochepa kwa miyezi ingapo ndipo Mulungu akugwiritsa ntchito nyengoyo kuti amuthandize.

Kupereka ndi mdalitso umene superekedwa kwa olemera okha. Kaya tili ndi zochepa kapena tili ndi zochulukira, chidzikhala chinthu chofunika komanso chokhumba chatu kuti tipereke chopereka chatu kwa Ambuye, popeza lye amatipatsa. Zoonadi sitingapereke koposa mmene Ambuye amatipatsira.

Michael W. Smith

January 2017

Zambiri Zali pa

INTANETI

Mukafuna kutipeza

pa intaneti, mulembe

www.thegospeltruth.org

kuti mudzilandira

makalata athu kapenanso

kuti muone. makalata

akale.

Kugwiritsa ntchito ndalama za chopereka cha Mpingo

Ophunzira anali otanganidwa ndi kulalikira mau a Mulungu and analangiza anthu kuti “yang’anani mwa inu amuna asanu ndi awiri a mbiri yabwino, odzala ndi Mzimu ndi nzeru, amene tikawaike asunge ntchito iyi.” (Machitidwe 6:2-3). Atumiki ndiwo amuna amene baibulo limanena kuti ndi oyenera kuti adziyang’anira zochitika za pa mpingo. Ndi kofunikira kukhala wokhulupirika ndi woona mtima.

Mwa ulemu wake, si koyenera kuti mtumiki wa Uthenga Wabwino adzigwira ndalama zoyendetsera mpingo. Chikhoza kukhala chanzeru kuti mbusa akhale asakudziwa amene akupereka koma kuti wapereka zingati, poopa kuti akhoza kuchita zinthu mosakhala bwino atadziwa zimenezi.



NTCHITO NDI MPHOTHO YAKE

Yesu anati, “Patsani, ndipo kudzapatsidwa kwa inu; muyeso wabwino, wotsen-dereka, wokuchumuka, wosefukira” (Luka 6:38). Pali mdalitso waukulu umene anthu ambiri amasemphana nawo pamene akanika kupereka modzikhuthula kwa Ambuye. Miyoyo ya Akhristu iyenera kudziwika ndi mitima yao yokonda kupereka.

Pali anthu ambiri amene ali osowa, pali ntchito yolalikira uthenga wabwino ndipo pali antchito a pampingo. Zonsezi zimafuna thandizo la chuma: “Lamulo langa ndi ili, kuti mukondane wina ndi mnzake, monga ndakonda inu” (Yohane 15:12). Paulo anamuza Timoteo kuti iwo amene achita ntchito yabwino, amene ali okonzeka kugawira kwa ena ndi kudziyikira maziko olimba kuti potero akagwiritsitse moyo wosatha (I Timoteo 6:18-20).

KUSANTHULA MAU A MULUNGU

MUTU: CHAKHUMI MU BAIBULO NDI KUPEREKA

Mau a Mulungu: *M’zinthu zonse ndinakupatsani chitsanzo, chakuti pogwiritsa ntchito, kotero muyenera kuthandiza ofooka ndi kukumbuka mau a Ambuye Yesu, kuti anati yekha, Kupatsa kutidalitsa koposa kulandira.* —Machitidwe 20:35

Kunena mwachidule: Chakhumi chinali chopereka cholamulidwa mu Chipangano Chakale. Chipangano Chatsopano chinabweretsa mwambo wopereka mwaufulu, modzikhuthula, komanso kuchokera pansu pa mtima. Kupereka mu Chipangano Chatsopano sikutengera mulingo wa zimene ulinazo koma chifukwa cha chikondi ndi kudzipereka kwa mzimu wa munthu.

I. Chakhumi Lisanabwere Lamulo

- A. Genesis 14:17-20 Abrahamu anapereka chakhumi kwa Melkizedeki.
- B. Genesis 28:20-22 Yakobo analonjeza kupereka chakhumi kwa Mulungu.

II. Chakhumi pansu Lamulo la Mose

- A. Levitiko 27:30-33 Chakhumi cha pa zakumunda ndi ziweto chilamulidwa ndi Mulungu.
- B. Numeri 18:21-24 Gawo limodzi la magawo khumi ndicho chakhumi cha Alevi.
- C. Duteronomo 14:22-23 (12:6-7) Kulamulira chakhumi chachiwiri.
- D. Duteronomo 14:28-29 (26:12-13) Kukhazikitsa chakhumi cha osauka.
- E. Malaki 3:8-9 Israeli anamulanda Mulungu.

III. Chilamulo cha Mose ndi chopandanso ntchito (onani Kalata ya No. 18)

- A. Ahebri 8:6-13 Pangano latsopano lakhazikitsidwa.
- B. Mateyu 23:23 Yesu adzudzula atsogoleri opereka Chakhumi.
- C. Aroma 7:6 Kumasulidwa ku Lamulo.

IV. Kupereka mu Chipangano Chatsopano

- A. II Akorinto 9:6-7 Mokondwerera, kukhazikitsa zopereka zaufulu.
- B. Yakobo 2:14-18 Chizindikiro cha chikhulupiriro choona.
- C. Aefeso 4:28 Gwirani ntchito kuti mupereke.

V. Njira Yovomerezeka ya Kupereka

- A. Mateyu 6:1-4 Mosaonetsera.

- B. II Akorinto 8:1-5 Modzikhuthula, mwa kufuna kwanu (Marko 12:41-44).

VI. Tipereke Mochuluka Bwanji

- A. II Akorinto 9:7 Monga mwatsimikizira mumtima mwanu.
- B. I Akorinto 16:1-2 Monga mmene Mulungu wakudalitsirani.
- C. Machitidwe 11:29 Monga mmene mungathere.
- D. Machitidwe 5:1-11 Chisankho cha munthu payekha (v.4).

VII. Perekani kwa Osowa

- A. I Timoteo 5:16 Azimayi amasiye.
- B. Yakobo 1:27 Ana amasiye ndi opanda bambo.
- C. Aroma 15:25-26 Oyera mtima osauka. (Machitidwe 11:27-29)
- D. Agalatiya 6:9-10 A m’banja la chikhulupiriro.
- E. Yakobo 2:14-18 Amaliseche ndi osowa pokhala.

VIII. Perekani ku Utumiki

- A. I Akorinto 9:7-14 Musayimange pakamwa ng’ombe.
- B. Agalatiya 6:6 Thandizani aphunzitsi.

IX. Madalitso a Kupereka

- A. Machitidwe 20:35 Kupereka ndi kodalitsika koposa.
- B. Luka 6:38 Patsani ndipo mudzapatsidwanso.
- C. Afilipi 4:18 Kumakondweretsa Mulungu.
- D. I Timoteo 6:18-19 Moyo wosatha.

Kumaliza: Munalandira kwaulere, patsani kwaulere. —Mateyu 10:8b

Chakhumi mu Baibulo ndiponso Chopereka

Mbiri ya Chakhumi

Chakhumi ndi chiphunzitso cha Chipangano Chakale chimene chinachotsedwa ndipo mmalo mwake munabwera chopereka chaufulu ndi chosakakamiza cha kwa Ambuye. Nkoyenera kuti tidziwe ndi kumvetsetsa za mbiri ndi chimene malemba amaphunzitsa za phunziroli.

Lamulo la Mose lisanaperekedwe, pali nthawi ziwiri zimene Chakhumi chinaperekedwa. Pa Genesis 14:17-20, Abrahamu anapereka chakhumi kwa Melkizedeki, mfumu komanso wansembe wa ku Salemu. Chakhumichi sichinachokere ku ndalama chake kapena ku phindu la zakumunda koma chinachokera ku zofunkha za kunkhondo. Pa Genesis 28:20-22, Yakobo anapanga lumbiro kwa Mulungu pamene analonjeza kuti adzapereka kwa Mulungu gawo limodzi la magawo khumi a zimene Ambuye ati adzampatse. Mu nyengo zonsezi, si Mulungu amene anapereka lamulo la chakhumi, koma anthu anapereka mwakufuna kwawo komanso ngati yowonetsa kudzipereka kwawo.

Lamulo la Mose

Pansi pa lamulo la Mose, Chakhumi chimalamulidwa ndi Mulungu. Chakhumi cha mu Chipangano Chakale chinali chosiyana ndi mmene mipingo yambiri ya masiku ano imanenera. Malingana ndi Levitiko 27:30-32, Chakhumi chinali pa za malimidwe ndipo chimaperekedwa pa zoweta ndiponso zakumudza osati pa zolandira ngati malipiro.

Zopereka zosiyanasiyana za Chakhumi zimene zimalamulidwa mu Chipangano Chakale

Kuposera apo, ngakhale kuti chakhumi chimayimira 10% ya zinthu zilizonse, panali magawo angapo a Chakhumi amene amayenera kuperekedwa malingana ndi malamulo a m'Chipangano Chakale. Chifukwa cha ichi, munthuyo amapereka koposera 10% monga mmene zimanenedwera masiku ano. Ngakhalebe pali kusiyana pa kamvedwe ka nkhanayi monga mmene amalambulira malamulo a Mose, panali muyeso wakuti zisachepere 20% (kapenanso chimodzi mwa zinthu zisanu zilizonse) zimene zimayenera kuperekedwa.

Chakhumi cha Alevi

Alevi samapatsidwa malo ngati cholowa chawo mu dziko la Israyeli monga momwe amachitira mafuko ena chifukwa Aleviwo amatumikira anzawo pa nkhani zokhudza chipembedzo. Chakhumi cha chaka choyamba, chakhumi cha Alevi chimalamulidwa kuti chidziperekedwa pofuna kuthandizira Alevi ndi ansembe kuti adzitha kudzipereka zosowa za pa moyo wawo. “Ndipo taonani,

ndawaninkha ana a Levi limodzi la magawo khumi mwa zonse m'Israele, likhale cholowa chao, mphotho ya pa ntchito yao alikuichita” (Numeri 18:21). Alevi ndi ansembe amapatsidwa chakhumi ngati chipukuta misozi chifukwa cha ntchito ndi kupereka nsembe zimene amachita.

Chakhumi cha pa Nthawi ya Chikondwerero

Panalinso chakhumi chachiwiri, chakhumi chachikondwerero, chimene chimalamulidwa kuti chibweretsedwe ku chihema chokomanako kapena ku Kachisi chifukwa cha maphwando a zipembedzo ndi zikondwerero mu Israyeli. “Muzipereka ndithu limodzi la magawo khumi la zipatso zonse za mbeu zanu, zofuma kumunda, chaka ndi chaka. Ndipo muzidye pamaso pa Yehova Mulungu wanu, m'malo m'mene asankhamo lye, kukhalitsamo dzina lake; limodzi la magawo khumi la tirigu wanu, la vinyo wanu, ndi la mafuta anu, ndi oyamba kubadwa a ng'ombe zanu ndi a nkhosa ndi mbuzi zanu; kuti muphunzire kuopa Yehova Mulungu wanu masiku onse” (Duteronomo 14:22-23). Onse apabanja pamodzi ndi antchito awo amadya chakudya chochokera ku chakhumichi. Inali nthawi ya chisangalalo ndipo chakudya cha alendo opita ku Yerusalemu katatu pa chaka chimachokera ku chakhumi chimenechi. Chakhumi ichi chinali chowonjezera pa chakhumi choyamba chija.

Chakhumi cha Osauka

Pa Duteronomo 14:28-29 ndi pa 26:12-13 anapereka malangizo a chachikhumi chachitatu, chakhumi cha osauka. Chakhumichi sichimaperekedwa chaka ndi chaka. Koma chimaperekedwa chaka chachitatu chilichonse chothandizira alendo, akunja, ana amasiye ndi amayi amasiye. Pali mtsutso waukulu pakati pa ophunzira a Baibulo ngakhale pakati aphunzitsi a Chiyuda ngati chakhumi chachitatutchi chinali chapadera kusiyana ndi chakhumi chachiwiri chija kapena ngati chinali gawo limodzi la chakhumi chachiwiri cho komanso ngati chimaperekedwa kwa osauka m'chaka chachitatu kapena chachisanu ndi chimodzi cha nyengo yakupumula. Nkofunika kudziwa kuti chakhumi chimapita kwa Alevi, chachiwiri chimapita ku Yerusalemu ndipo chachitatu chinali chothandizira onse osauka onse amene ali “m'midzi mwanu” (Duteronomo 26:12). Chachikhumi cha osauka chinali kulamulidwa kuti chithandizire zosowa za osauka “kuti Yehova Mulungu wanu akakudalitseni mu ntchito zonse za dzanja lanu muzichitazi” (Duteronomo 14:29).

(Yapitirira pa tsamba 6)

(Kuchokera pa tsamba 5)

Kuwonjezera pa chopereka chilichonse chaufulu chimene chimaperekedwa, chakhumi cha zakumunda ndi zoweta chikadamakwana mosachepera 20%-23.3%. Panalibe kusankha pa zopereka za chakhumi izi ndipo zinali kulumulidwa ndi Yehova Mulungu. M’buku la Malaki 3:8-9, mneneri anawafunsa anthu kuti, “Kodi munthu adzalanda za Mulungu? Ndipo inu mundilanda Ine. Koma mukuti, Takulandani zotani? Limodzilimodzi la magawo khumi, ndi zopereka.” Anthu a Israele amamulanda Mulungu zimene zinali zake ndi kale lomwe malingana ndi Malamulo amene anaperekedwa kwa Mose.

Pangano la Chipangano Chakale Linasinthidwa ndi lina

Monga mmene umakhalira msonkho waboma kapena wachipembedzo, Chakhumi chimene chimalandiridwa m’nthawi ya chilamulo cha Mose chimathandizira kukwaniritsa zofunikira m’boma la Israele limene mfumu yake inali Mulungu mwini. Zofunikirazo zinali monga za m’udzi, mu chipembedzo, za boma.

Ngakhale palibe kukayika konse kuti Chakhumi chinali lamulo mu Chipangano Chakale, kusiyana ndi zophunzitsa za alaliki onyenga ambiri, Chakhumi sichiphunzitsidwa mu Chipangano Chatsopano. Pamene Yesu Khristu anabwera, anadzachita pangano latsopano ndi anthu a Mulungu ndipo pangano lakale linali litapita (Ahebi 8:6-13). Vesi 8 ikunena kuti: “Taonani, akudza masiku, anena Ambuye, Ndipo ndidzapangana pangano latsopano ndi nyumba ya Israele.” Dongosolo la lamulo la Chakhumi linathetsedwa monga mmene anachitira ndi Kusungu Sabata, nsembe za nyama, ndi kupembedza kwa thupi ndi zina zotere.

Yesu analankhula za Chakhumi pamene amadzulula atsogoleri a chipembedzo amene anali okhululupirika popereka chakhumi koma samalabadirako zazikulu zenizeni za malamulo (Mateyu 23:23; Luka 11:42). Chakhumi chinali kuchitika pakati pa Ayuda m’nthawi ya utumiki wa Khristu chifukwa Israyeli anali akadali pansu pa chilamulo ndipo dongosolo lonse la chipulumutso linali lisanafike pachimake mpaka pa tsiku la Pentekoste.

Mfundo zina za mu Chipangano Chakale zinabwezeretsedwanso koma zambiri zinakwaniritsidwa mu mkhalidwe wina wapamwamba umene uchokera pa ubale waumunthu ndi wodzipereka mwa Yesu Khristu. Chilungamo chenicheni sichikhazikika pa kupereka kwakuti “ndipereka limodzi la magawo khumi la zonse ndili nazo” (Luka 18:12) koma pa chisomo chopulumutsa cha Yesu Khristu. “Koma tsopano tinamasulidwa kuchilamulo, popeza tinafa kwa ichi chimene tinagwidwa nacho kale; chotero kuti titumikire mu mzimu watsopano, si m’chilembo chakale ai” (Aroma 7:6).

Kupereka mu Chipangano Chatsopano

Ngakhale Chipangano Chatsopano sichiphunzitsa za Chakhumi cha ndalama, Chipangano Chatsopano chimanena kwambiri za kupereka.

Chikhristu chimatsamira pa kutumikira Mulungu mwaufulu ndi mwachikondi. Chiphunzitsa cha Chipangano Chatsopano chonena za kupereka chikupezeka mwachidule mu malangizo a mtumwi Paulo ku mpingo wa ku Korinto. “Koma *nditi* ichi, kuti iye wakufesa mouma manja, mouma manjanso adzatuta. Ndipo iye wakufesa moolowa manja, moolowa manjanso adzatuta. Yense *achite* monga anatsimikiza mtima, si mwa chisoni kapena mokakamiza, pakuti Mulungu akonda wopereka mokondwerera” (2 Akorinto 9:6-7).

Kupereka mwaufulu mwa Kufuna kwathu

Kusiyana ndi chakhumi, zopereka zathu za kwa Mulungu zina zonse ziyenera kukhala “zopereka zaufulu.”



Chilichonse chimene Mkhristu alinacho chidzipatulidwa kwa Ambuye.

Malingana ndi mmene ananenera wolemba wina dzina lake Adam Clarke, Ayuda anali ndi mabokosi awiri m’kachisi oyikamo zothandizira osauka. Bokosi la “zoyenera kuperekedwa” limene zopereka zimaponyedwamo malingana ndi lamulo la chakhumi. Bokosi lachiwiri linali la la zopereka zaufulu pamene anthu amapereka malingana ndi ndi chikondi komanso mtima wao pa Mulungu. Mu Chipangano Chatsopano, bokosi la Chakhumi linachotsedwa ndipo zopereka zonse zimayenera kuperekedwa monga mmene wafunira mumtima mwake—osati chinthu chimodzi pa khumi kapena pa zisanu monga mmene amalambulira.

Udindo wa Kupereka

Ufulu ku lamulo la Chakhumi supangitsa kuti anthu asamapereke. Chilichonse chimene Mkhristu alinacho chiyenera kupatulidwa kwa Ambuye. Ngakhale kuti palibe mulingo uliwonse wa kaperekedwe, komabe pali udindo wakuti tidzipereka mowolowa manja, modzikhuthula, komanso ndi mtima wokondwerera. Pa nkhani zokhudza chuma, kupereka kwa Ambuye chidzikhala chinthu choyambirira. Zopereka zaufulu zidziperekedwa pofuna kuthandiza utumiki, ntchito ya uthenga wabwino, osauka ndi zina zotere. Tiyeni tiganizire “ndi kukumbuka mau a Ambuye Yesu, kuti anati yekha, Kupatsa kutidalitsa koposa kulandira” (Machitidwe 20:35). Zopereka zochokera pansu pa mtima ndi nsembe zovomereka ndi zokondweretsa kwa Mulungu (Afilipi 4:18).

—mws



Kodi ndi kupereka kotani kwa ChiKhristu kumene kuli kovomerezeka?

“Koma iwe popatsa mphatso zachifundo, dzanja lako lamanzere lisadziwe chimene lichita dzanja lako lamanja” (Mateyu 6:1-4). Ana a Mulungu sakuyenera kupereka kuti anthu awadziwe kapena kuwayamikira, koma akuyenera kupereka monga mmene angathere, mosafuna kuti adziwiwe ndi mwachinsinsi komanso ndi mtima wodzichepetsa ndi wachikondi chochuluka.

Kodi nkoyenera kuti mpingo udzitolera chopereka, ngati zili choncho, udzichita motani?

Sikofunikira kokha koma ndi koyenera ndithu kuti mpingo udzikhala ndi dongosolo lakuti anthu adzipereka zopereka zao kwa Ambuye. Paulo adalangiza mpingo wa ku Korinto kuti: “Koma za chopereka cha kwa oyera mtima, monga ndinalangiza Mipingo ya ku Galatiya, motero chitani inunso. Tsiku loyamba la sabata” (I Akorinto 16:1-2). Mpingo umalangizidwa kuti usonkhane ndi kutolera chopereka pa tsiku loyamba la sabata, limene linali tsiku lopembedza. Kupereka ndi gawo limodzi la kupembedza kwathu komanso utumiki wa chikondi chatu kwa Ambuye ndipo izi sitiyenera kuziyiwalala. Malemba sakulangiza mwatchutchutthu mmene chopereka chimayenera kutoleredwera. Chikuyenera kukhala chopereka chafulu ndipo chisawamange anthu m’goli. Ndi kofunikira kuti tisatsate chiphunzitso chimodzi pa za mmene tingayendetse choperekacho – kaya ndi kabokosi ka chopereka koyikidwa posaonekera kapena njira ina yake

yolandirira chopereka ya onse. Ufulu komanso kusungu chinsinsi ndi zofunikira. Tilimbikitse anthu kukhala odzichepetsa pa kupereka kusiyana ndi mchitidwe womabetcha pa chopereka umene mipingo ina imagwiritsa ntchito ikafuna kutolera ndalama.

Kodi Mkhristu apereke moyandikana bwani komanso mochuluka bwani?

Baibulo limaphunzitsa kuti Mkhristu apereke monga “Yense achite monga anatsimikiza mtima” (II Akorinto 9:7). Pa I Akorinto 16:2 akuti, “yense wa inu asunge yekha, monga momwe anapindula.” Mkhristu ayenera kupereka nthawi iliyonse imene Mzimu wakakamiza mtima wake kupereka komanso mulingo uliwonse. Ngakhale sitili panso pa lamulo la



Chakhumi, pangano lakale linali ngati namkungwi. Nkofunikirabe kupereka kwa Ambuye poyamba kuposa zina zonse, motsimikiza mtima komanso pafupipafupi. Nkoyenera ndithu kutsimikiza kwa Ambuye ndikukhala okhulupirika ku icho, komanso osamuyikira Mulungu malire pamene watifulumiza kuti tipereke moposera kale. Kwa anthu ena amene salandira ndalama zochuluka, kupereka modzikhuthula kukhoza kutanthauza ndalama zochepa. Koma kwa olemera, mlingo wa kupereka chuma modzikhuthula ukhoza kukhala oposer pa 20%. “Ndipo ophunzira, yense monga anakhoza, anatsimikiza mtima kutumiza zothandiza abale” (Machitidwe 11:29).

Kodi zopereka ziperekedwe kwa ndani?

Kupereka sikuyenera kungochitika kudzera

mu mpingo wokha, komanso kuyenera kuchitika chifukwa cha malamulo amene aperekedwa m’Mau a Mulungu. Zopereka ziyenera kuperekedwa pofuna kukwaniritsa udindo wa m’Baibulo wothandiza osauka ndi amayi amasiye (I Timoteo 5:16), ana amasiye (Yakobo 1:27), ndiponso pofuna kuthandizira utumiki ndi ntchito ya Mulungu.

Zopereka zimatoleledwa ku Makedonia ndi Akaya pofuna kuthandiza oyera mtima osauka amene anali ku Yerusalemu (Aroma 15:25-26). Thandizo limatumizidwa kwa abale a ku Yudeya (Machitidwe 11:27-29). Mtumwi Yakobo ananepo za kufunikira kwakuti tionetsere chikhulupiriro chatu pothandiza amaliseche ndi ausiwa (Yakobo 2:14-18). Udindo wothandiza osauka

umayamba ndi a m’banja la chikhulupiriro ndipo umakula kuchokera pamenepo (Agalatiya 6:9-10). Malemba amanena momveka bwino zakuti anthu amagwira ntchito ndi manja awo kuti potero athe kupereka kwa iwo omwe angafune thandizo (Aefeso 4:28). Palinso maudindo ena ngati kulipila mabilu a mpingo monga madzi, magetsi, mafoni komanso kusamalira malo opembedzerapo.

Mu Chipangano Chakale, kunali koyenera kuti Aisrayeli apereke Chakhumi pofuna kuthandiza ntchito

ya ansembe ndi Alevi. Mu Chipangano Chatsopano, oyera mtima amaphunzitsidwa mmalo osiyanasiyana kuti athandize utumiki ndi chuma. “Usapunamitsa ng’ombe pakupuntha iyo dzinthu...Ngati takufeserani inu zauzimu, kodi nchachikulu ngati ife tituta za thupi lanu?” (I Akorinto 9:7-11). Ngati mukuphunzitsidwa Mau a Mulungu, muthandizeni iye amene amakuphunzitsani inu mu zabwino zonse (Agalatiya 6:6). Wogwira ntchito ndi woyenera malipiro ake kaya iye ndi mbusa, mlaliki, wogwira ntchito ya Mishoni ndi ena otere. Ndi udindo wa oyera mtima kuthandiza mosakakamidwa iwo amene akugwira ntchito mu ufumu wa Mulungu.



KODI MUKUDZIWA?

Ndodo yoyezera Chakhumi

“Ambuye anakhazikitsa mfundo ya Chakhumi pakati pa Aisraele pofuna kulozera za njira imene abusa a nkhosa amawerengera nkhosa zawo [Levitiko 27:32]. Pamene nkhosa zimawetedwa kupita ku khola kwao usiku, mbusa amayimirira pambalipo ali ndi ndodo imene inali yopakidwa utoto. Amapaka ndi utoto uja nkhosa iliyonse yachikhumi pamene zimaowa m’khola muja. Izi zimamuthandiza mbusayo kuti awerengetsere mosavuta ndi kuzindikira ngati zina zinasowapo. (Knight, George W. 2007. *Bible Customs & Curiosities*, p. 56).



Mau a pa
Nyengo Yake

Kulandira cholowa chifukwa cha Uthenga Wabwino

KUTI MUTIPEZE

The Gospel Truth
PO Box 2042
Nixa, MO 65714
USA
Email:
editor@thegospeltruth.org

CHIYERO CHA KWA AMBUYE

Kodi simudziwa kuti iwo akutumikira za Kachisi amadya za m’Kachisi, ndi iwo akuimira guwa la nsembe, agawana nalo guwa la nsembe? Chomwechonso Ambuye analamulira kuti iwo amene alalikira Uthenga Wabwino akhale ndi moyo ndi Uthenga Wabwino.
—I Akorinto 9:13-14

Atumiki a Mulungu asadzipangire chuma pofuna kutumikira zosowa zawo za thupi koma akhulupirire mwa Mulungu amene anawayitana kuti akatumikire. Nkofunikira kuti atumiki asagwire ntchito kuti apeze phindu lopyolera muyeso kapena kuti alandire malipiro koma akhale ndi mtima wotumikira komanso wofuna kumangirira miyoyo ina.

Ngakhale pamene atumiki a uthenga wabwino amayenera kuyang’ana kwa Mulungu osati kwa anthu, pali udindo umene waperekedwa kwa anthu. Mtumwi Paulo amakumbutsa mpingo wa ku Korinto za mmene iye anagwirira ntchito ndi kudziperekera ku utumiki. M’masiku a m’mbuyowo, ansembe amayenera kutengako gawo la nsembe zimene zaperekedwa kuti adzipeza chakudya. Pamene amadikira pa guwa, amadyeranso paguwa pomwepo. Ndi mmenenso ziyenera kukhalira ndi atumiki athu lero.

Iwo amene amatumidwa ndi Khristu ndipo amayika miyoyo yao pa chiswe kuti alalikire uthenga ayenera kuthandizidwa ndi kulimbikitsidwa pamene akugwira ntchito yao. Ndi udindo wa okhulupirira kuti adzikhuthule ndi kupereka mowolowa manja kuti utumiki ukhazikike pa zenizeni za Mulungu komanso ukwanitse kugwira ntchito mosavuta m’ munda wauzimu umene akutumikira.



—mws